

MPHAMVU YA KUUKA KWA KHRISTU



Phunziro 8, August 22, 2026

“Ndipo ngati Khristu sanaukitsidwe, ndiye kuti kulalikira kwathu n’kopanda ntchito, ...Ndipo ngati Khristu sanaukitsidwe, chikhulupiriro chanu n’chopanda ntchito; mukanali mu machimo anu.!” (1 Akorinto 15:14-17, CCL)





Malinga ndi nzeru za Agiriki—zomwe zinachokera ku ziphunzitso za Plato—thupi, lomwe mwachilengedwe lake ndi loipa, ndi ngati ndende chabe ya moyo wamuyaya. Poganizira zimenezi, kodi kuuka kwa thupi kunali kutanthauza chiyani kwa Agiriki kapena Aroma?

Pachifukwa chimenechi, gawo lina la mpingo wa ku Korinto linakana mfundo yakuti kuuka kwa akufa ndikotheka. Paulo akukamba nkhani imeneyi m'mutu 15 wa kalata yake yoyamba yopita kwa Akorinto.

Iyi si nkhani yopepuka. Kuuka kwa akufa kuli ndi kugwirizana kwakukulu ndi chipulumutso. Ngati kulibe kuuka kwa akufa... kodi pali phindu lanji kulalikira uthenga wabwino?



Kuuka kwa Yesu

Kodi kuuka kwa akufa kunachitikadi mu mbiri?

(1 Akorinto 15:1-11)

Zotsatira za kuuka kwa Yesu

Kodi zikanakhala bwanji Khristu akanapanda kuuka kwa akufa?

(1 Akorinto 15:12-19)

Ndichiyani chimatsimikizira za kuuka kwa akufa?

(1 Akorinto 15:20-34)

Kuuka kwathu kwa akufa

Kodi tidzaukitsidwa ndi thupi lotani?

(1 Akorinto 15:35-49)

Kodi tidzaukitsidwa liti?

(1 Akorinto 15:50-58)


+

•

○

KUUKA KWA

YESU



KODI KUUKA KWA AKUFA KUNACHITIKADI MU MBIRI?

“Pakuti chimene ndinalandira ndinapereka kwa inu monga chofunika kuposa zonse, kuti Khristu anafera zoyipa zathu monga mwa Malemba, 4kuti anayikidwa m’manda, kuti anaukitsidwa tsiku lachitatu monga mwa Malemba;” (1 Akorinto 15:3-4)

Asanayankhe mafunso kapena kukayikira komwe anthu a ku Korinto anali nako pankhani ya kuuka kwa akufa, Paulo akuwakumbutsa mmene uthenga wabwino umagwirira ntchito (1 Akorinto 15:1-2):

Umalalikiridwa



Umalandiridwa



Munthu amalimbikira mmenemo



Chipulumutso chikupezeka



Nanga uthenga wabwino umenewu umalalikidwa ndi wotani? (1 Akorinto 15:3-4)

Khristu Anafera machimo athu



Khristu anaikidwa m’manda



Khristu Anauka tsiku la chitatu



Nanga timadziwa bwanji kuti kuuka kwa Yesu kunachitikadi mu mbiri? Ndani anaona Yesu atauka? (1 Akorinto 15:5-8)

Petulo ndi
Ophunzira Khumi
ndi Awiri




Abale ndi alongo
oposa 500



Yakobo ndi atumwi



Paulo “olephera”




Paulo akufotokoza momveka bwino kuti uthenga wabwino ndi ntchito ya Mulungu imene inachitika ‘monga mwa Malemba.’ Ndiko kuti, ndi dongosolo limene Mulungu anakonzeratu, ndipo kuukitsidwa kuli ndi gawo lofunika kwambiri m’dongosolo limeneli. Kodi pali amene akukayikira? Afunse anthu amene anaona zimenezi ndi maso awo, amene pa nthawiyo anali akadali ndi moyo!

ZOTSATIRA ZA KUUKA KWA YESU



KODI ZIKANAKHALA BWANJI KHRISTU AKANAPANA KUUKA KWA AKUFA?

"Ndipo ngati Khristu sanaukitsidwe, ndiye kuti kulalikira kwathu n'kopanda ntchito, ndipo chikhulupiriro chanu n'chopandanso ntchito." 1 Akorinto 15:14



Kukana kuti kuukitsidwa kwa akufa kungatheke kumatsutsana ndi chikhulupiriro cha Chikhristu, chifukwa 'ngati kulibe kuukitsidwa kwa akufa, ndiye kuti Khristunso sanauke' (1 Akorinto 15:12–13). Ndipo ngati Yesu sanauke...

Kulalikira uthenga wabwino ndikopanda pake (1 Akorinto 15:14a)

Chikhulupiriro chathu ndichachabe (1 Akorinto 15:14b) [chopanda phindu] (1 Akorinto 15:17a)

Ndife mboni zabodza (1 Akorinto 15:15)

Tikadali m'machimo athu (1 Akorinto 15:17b)

Anthu amene anamwalira sadzakhalanso ndi moyo (1 Akorinto 15:18)



Popanda kuuka kwa akufa, Yesu akanangokhala munthu wolungama amene anaphedwa popanda chifukwa, koma wosatha kupulumutsa. "Koma tsopano Khristu wauka kwa akufa" (1 Akorinto 15:20a). Tili ndi Mpulumutsi WAMOYO.

Pachifukwa chimenechi, uthenga wabwino uli ndi tanthauzo; chikhulupiriro chathu chilinso ndi tanthauzo; ndife mboni zokhulupirika; machimo athu akhululukidwa; ndipo amene anamwalira ali mwa Khristu adzaukanso.



NDICHIYANI CHIMATSIMIKIZIRA KUUKA KWA AKUFA?

**“Koma n’zoonadi kuti Khristu anaukitsidwa kwa kufa, chipatso choyamba cha onse ogona tulo.”
(1 Akorinto 15:20)**



Mfundo yoyamba imene kuukitsidwa kwa Yesu kumatitsimikizira ndi yakuti, tonse amene tavomera dongosolo la chipulumutso—kuyambira Adamu mpaka kumapeto kwa dziko—ngati titamwalira, tidzaukanso ndi kukhala ndi moyo (1 Akorinto 15:20–23).

Kodi chidzachitike ndichiyani tikadzaukitsidwa? Pogonjetsa imfa, Yesu adzakhala atagonjetsa adani ake onse (1 Akorinto 15:25-26). Kenako, Yesu adzaika chilichonse pansi pa Atate, kuti “Mulungu akhale zonse mu zonse” (1 Akorinto 15:24, 28).

Kuwonjezera pa zitsimikizo zamtsogolo izi, Paulo akutipatsa zitsimikizo ziwiri zomwe zimakhudza miyoyo yathu ya tsiku ndi tsiku:



1 Akorinto 15:30-32

Ndikoyenera kulalikira uthenga wabwino, ngakhale zitakhala zovuta kapena zoopsa.



1 Akorinto 15:33-34

Ndi bwino kukhala ndi moyo wogwirizana ndi mfundo za m’Baibulo.

+
**KUUKA KWATHU
KWA AKUFA**



KODI TIDZAUKITSIDWA NDI THUPI LOTANI?

“Zidzaterenso pamene akufa adzauka. Thupi loyikidwa m’nthaka ngati mbewu limavunda, koma likadzauka lidzakhala losavunda.” (1 Akorinto 15:42)

Mafanizo okhudza thupi loukitsidwa:

Matupi a zomera (1 Akorinto 15:35-38)

Mbewu imafesedwa



Zam’munda zimakolole-dwa



Mulungu amapatsa chomera chilichonse thupi limene lye akufuna.



Matupi a mnofu (1 Akorinto 15:39)

Matupi a anthu



Matupi a nyama



Matupi a nsomba



Matupi a mbalame



Matupi akumwamba (1 Akorinto 15:40-41)

Ulemerero wa dzuwa



Ulemerero wa mwezi



Ulemerero wa nyenyezi



Aliyense ali ndi ulemerero wake (kuwala kwake)



KODI TIDZAUKITSIDWA NDI THUPI LOTANI?

“Zidzaterenso pamene akufa adzauka. Thupi loyikidwa m’nthaka ngati mbewu limavunda, koma likadzauka lidzakhala losavunda.” (1 Akorinto 15:42)

Kodi pali kusiyana kotani pakati pa thupi limene tili nalo panopa ndi thupi limene tidzakhale nalo tikadzaukitsidwa? (1 Akorinto 15:42-44)

Thupi la panopa

lowonongeka

Lopanda ulemu

Lopanda mphmvu

Chinyama


Thupi loukitsidwa

Losawonongeka

Laulemerero

Lamphmvu

ZaUzimu




Adamu anali ndi thupi la padziko lapansi lino, pamene Adamu wachiwiri [Yesu] anali nalo la kumwamba. Pa nthawi ya kuuka kwa akufa, thupi lathu lidzasinthidwa n’kukhala lofanana ndi thupi la Khristu; ndiye kuti lidzakhala losawola, la ulemerero, lamphamvu, la mzimu, komanso la kumwamba (1 Akorinto 15:45-49).

KODI TIDZAUKITSIDWA LITI?

"Tamverani, ndikuwuzeni chinsinsi. Tonse sitidzagona tulo, koma tonse tidzasandulika.—." (1 Akorinto 15:51)

Asanafotokoze nthawi ya kuuka kwa akufa ndi zimene zidzachitikire matupi athu pa nthawiyo, Paulo akunena kuti "thupi ndi mwazi sizingathe kulowa mu Ufumu wa Mulungu" (1 Akorinto 15:50). Kodi zimenezi zikutanthauza kuti tikadzaukitsidwa sitidzakhala ndi thupi lenileni?

Mawu akuti "thupi ndi mwazi " nthawi zonse amagwiritsidwa ntchito kutanthauza "munthu" (Mateyu 16:17; Agalatiya 1:16; Aefeso 6:12; Aheberi 2:14). Apa Paulo akufananiza zinthu ziwiri: anthu okhala padziko lapansi = kuwola; anthu okhala kumwamba = osawola. Pano tili ndi thupi limene limawola, choncho sitingathe kupita nalo kumwamba mmene lilirimu.



Pa Kubwera Kwachiwiri, thupi lowola lidzasinthidwa kukhala thupi losawonongeka, monga thupi limene Yesu anauka nalo (1 Akorinto 15:51-55; Luka 24:36-40).

Kwa amene agona mwa Yesu, zidzakhala ngati kuti pangodutsa kanthawi kochepa kwambiri. Kamphindi kapitako anamva kuzizira kwa imfa, koma tsopano akuona kale Yesu akubwera (1 Akorinto 15:52).



“Kuukitsidwa kwa Yesu kunali chitsanzo cha kuukitsidwa komaliza kwa onse amene agona mwa Iye. Thupi loukitsidwa la Mpulumutsi, mmene ankakhalira ndi kuchitira zinthu, ndiponso kamvekedwe ka mawu ake, zonsezi zinali zodziwika bwino kwa otsatira ake. Momwemonso, amene agona mwa Yesu adzaukanso. Tidzawazindikira anzathu monga momwe ophunzira anamuzindikirira Yesu. Ngakhale kuti m’moyo uno wa imfa matupi awo angakhale opunduka, odwala, kapena owonongeka, akadzaukitsidwa ndi matupi aulemerero, aliyense adzakhalabe munthu yemweyo ndipo adzadziwika bwino. Pankhope zawo zonnyezimira ndi kuwala kochokera pankhope ya Yesu, tidzazindikirabe nkhope za anthu amene timawakonda.”